Kalata ya No. 55

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

## KUITANIDWA KWA ANENERI

*"Ndatumanso kwa inu atumiki anga onse aneneri, ndalawirira ndi kuwatuma, kuti, Bwererani kuleka yense njira yake yoipa, konzani machitidwe anu..."*
— Yeremiya 35:15

Kuyambira pa masiku oyambirira a mbiri ya Israele, Mulungu anadzutsa anthu kuti alankhule mau ake kwa anthu. Kuitana kwa uneneri sikunayambe ndi chikhumbokhumbo cha anthu kapena luso lachibadwidwe; kunayamba ndi Mulungu mwiniwake. Iye anasankha chotengeramo chake, napereka uthenga, ndipo anatumiza mneneri kuti akaime m'malo mwake ndi kulengeza mau ake. Oyitanidawo ananyamula katundu wolemera amene sanasankhe, komabe sakanatha kuthawa.



"Masiku ano, Mulungu akufunafunabe amuna ndi akazi omwe adzamva liwu ake, nadzipereke ku chifuniro chake, ndi kulankhula choonadi chake modzichepetsa komanso molimba mtima."

Aneneri sanali onse ofanana. Ena anachokera m'mabwalo achifumu, pomwe ena anali alimi, abusa a ziweto, kapena antchito. Ena ochepa anali ophunzitsidwa bwino ndi ena ophunzira kwambiri; ena analibe zowayenereza zilizonse malingana ndi kuona kwa dziko lapansi. Umunthu wao unali osiyana; ena anali achifundo ndi olira, ena olimba mtima ndi oopsa, enanso anali odekha komanso osasunthika. Komabe, ngakhale anali osiyana, choonadi chinali chimodzi chomwecho chakuti: **Mulungu anawaitana.** Iye anaika mau ake m'kamwa mwawo ndipo mtolo m'mitima yawo.

Nthawi zambiri uthenga wao unali kukumana ndi kutsutsidwa. Iwo ankalankhula mu nthawi yamavuto, kupembedza mafano, chionongeko, komanso kusakhazikika kwa dziko. Iwo ankachenjeza za chiweruzo pamene anthuwo ankangokonda mau oziziritsa mtima. Iwo anali ngati mau a Mulungu ku mtundu woyendayenda, wobwerera m'mbuyo, nawalimbikitsa anthuwo kuti alape. Anatsogolera Israele kubwerera ku chilungamo pamene dzikolo linayamba kuchimwa. Anapereka chiyembekezo pamene chiyembekezo chimaoneka kuti chatayika, nawakumbutsa okhulupirika kuti Mulungu sanaiwale pangano lake. Aneneri ambiri ankanyozedwa ndi kunyozedwa; ankazunzidwa, kusungulumwa, ngakhale imfa chifukwa chomvera. Komabe, anakhalabe okhulupirika kwa Iye amene anawatuma.

Aneneri awa anali anthu, ngakhale anali apadera, osamvetsetsedwa, komanso okanidwa nthawi zambiri. Iwo anakumana ndi mantha, kutopa, kukhumudwa, ndi nthawi zovuta kwambiri. Ena anajejema, ena amadziona kuti ndi osakwanira, ndipo ena analimbana ndi udindo waukulu womwe unali pa iwo. Komabe Mulungu anawagwiritsa ntchito, osati chifukwa chakuti anali opanda chilema, koma chifukwa chakuti anali ofunitsitsa. Mphamvu yake inakhala yangwiro mu kufooka kwawo, ndipo uthenga wake unafalikira kudzera mu zotengera zooneka zosayenera zomwe zinamukhulupirira Iye.

Kuitana kwa uneneri sikunathere ndi Chipangano Chakale. Masiku ano, Mulungu akufunafunabe amuna ndi akazi omwe adzamva mawu ake, nadzipereke ku chifuniro chake, ndi kulankhula choonadi chake modzichepetsa komanso molimba mtima. Funso limene lili lofunika kwambiri kufikira lero ndilo lakuti: *"Ndidzatumiza yani, ndipo ndani adzatimukira ife?"* Yankho lathu ligwirizane ndi yankho la Yesaya lakuti: **"Ndine pano; munditumize ine."** ■


| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| Kuitanidwa Kwa Aneneri 1 | Aneneri ndi nthawi yawo 2 | Yesaya 3<br>Zefaniya, Habakuku, Yeremiya 4-5 | Ezekiele, Daniele 7 | Mika 8 |

# Aneneri ndi nthawi yawo

Mabuku a uneneri a m'Baibulo sanayikidwe mwandondomeko potsatira zaka zawo, ndipo zingakhale zovuta kudziwa chaka chenicheni chimene mneneri aliyense ananenera mu mbiri ya Israele. Mndandanda uli m'munsimu ukutipatsa chithunzithunzi chosavuta cha nthawi yomwe aneneri anatumikira, malingana ndi zolemba zawo; kuyambira asanatengedwe kunka ku ukapolo ku Babiloni, panthawi ya ukapolo, komanso atabwerera ku Yuda kuchoka ku ukapolo. Eliya ndi Elisa nawonso akuphatikizidwa chifukwa cha malo awo ofunikira mu nkhani yauneneri. Malemba amatchula za aneneri ena amene mautumiki awo anali ofunikira, ngakhale kuti zolemba zawo sizinasungidwe m'mabuku a aneneri.

| DZINA | ZAKA (BC) | DERA | NTHAWI YAKE |
|---|---|---|---|
| **Eliya** | 875-848 | Israele (Ufumu wa Kumpoto) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Elisa** | 848-800 | Israele (Ufumu wa Kumpoto) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Yoweli** | Zaka za m'ma 900 mpaka m'ma 500 (zosatsimikizika) | Yuda | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Amosi** | 760 | Israele (kuchokera ku Yuda) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Hoseya** | 755-715 | Israele (Ufumu wa Kumpoto) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Yesaya** | 740-686 | Yuda (Yerusalemu) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Mika** | 740-687 | Yuda (Moresheti) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Nahumu** | 663-612 | Yuda | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Zefaniya** | 640-621 | Yuda | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Habakuku** | 612-600 | Yuda | Asanatengedwe kunka ku ukapolo |
| **Obadiya** | pafupifupi 586 | Yuda | Kutengedwa ku ukapolo (koyamba) |
| **Yeremiya** | 626-586 | Yuda (Anatoti/Yerusalemu) | Asanatengedwe kunka ku ukapolo komanso nthawi ya ukapolo |
| **Maliro (Yeremiya)** | 586 | Yuda | Nthawi ya ukapolo |
| **Ezekiele** | 593-571 | Babiloni (Mtsinje wa Kebara) | Nthawi ya ukapolo |
| **Daniele** | 605-536 | Kuyambira ku Babiloni kupita ku Perisiya | Nthawi ya ukapolo |
| **Hagayi** | 520 | Yuda | Atabwerako ku ukapolo |
| **Zekaria** | 520-518 | Yuda | Atabwerako ku ukapolo |
| **Malaki** | 450-430 | Yuda | Atabwerako ku ukapolo |

*Zithunzi zonse ndi zongofanizira chabe.

*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA

# Aneneri a Chipangano Chakale

Aneneri a Chipangano Chakale anasankhidwa ndi Mulungu kuti alankhule mau ake nthawi yamavuto ndi chionongeko. Iwo anachenjeza za chiweruzo, nawaitanira anthu ku chilungamo, ndipo anapereka chiyembekezo cha kubwezeretsedwa. Anatsogoleranso ndi kulimbikitsa, nafunafuna kuwabwezetsa anthu kwa Mulungu. Miyoyo ndi mauthenga a aneneri zimapitiriza kutikumbutsa za chiyero cha Mulungu, chifundo chake, chiweruzo chake, ndi kukhulupirika kwake.

## YESAYA

### MNENERI WONENA ZA MESIYA



***MASIKU:*** Anatumikira pafupifupi 740–686 BC

***NTCHITO:*** Mneneri

***MALO:*** Yerusalemu; Yuda

***BUKU:*** Yesaya

***MITU:*** Chiyero, chiweruzo, kulapa, kubwezeretsedwa, Mesiya amene akubwera

Dzina la Yesaya (limatanthauza *"Ambuye ndiye chipulumutso"*) limasonyeza uthenga waukulu wa utumiki wake. Kuitanidwa kwa Yesaya ku utumiki wa uneneri kunabwera "m'chaka chimene Mfumu Uziya anafa," pamene anaona masomphenya a Ambuye m'kachisi (Yesaya 6:1-8). Anakhala ku Yerusalemu ndipo ananenera za ufumu wakum'mwera wa Yuda, womwe unali ndi mafuko a Yuda ndi Benjamini. Ufumu wakumpoto wa Israele unali wopembedza mafano kwambiri ndipo pamapeto pake unagwa m'manja mwa Asuri mu 722 BC.

Yesaya anatumikira pa nthawi ya ulamuliro wa mafumu awa: Uziya, Yotamu, Ahazi, ndi Hezekiya (Yesaya 1:1). Chifukwa chakuti ankakhala ku Yerusalemu ndipo ankacheza kwambiri ndi mafumu amenewa, zikuoneka kuti anali ndi ubale ndi bwalo lachifumu, ngakhale kuti Malemba safotokoza izi mwatsatanetsatane.

Yesaya anali wokwatira ndipo anali ndi ana aamuna osachepera awiri omwe maina awo anali ndi tanthauzo laulosi. Seari-Yasubu (*"otsala adzabwerera"*) ndi Mahara-salali-hasi-bazi (*"Kangaza kufunkha, fulumira kusakaza"*) zinali zizindikiro kwa dzikolo ndipo zinkasonyeza uthenga umene Mulungu adamupatsa (Yesaya 7:3; 8:1-4).

Yesaya anadzudzula Yuda chifukwa cha tchimo lawo ndipo anachenjeza za chiweruzo chomwe chikubwera. Dzikolo linayesedwa kudalira mgwirizano wandale, makamaka ndi Igupto, pamene Asuri anali kulamulira. Yesaya anawakumbutsa kuti palibe mtundu wachilendo umene ungawapulumutse; chitetezo chawo chokha chinali kukhulupirira Ambuye (Yesaya 31:1). Ananeneratu kuti tsiku lina Yuda adzatengedwa kupita ku Babiloni (Yesaya 39:6-7), uneneri umenewu unakwaniritsidwa zaka zoposa 100 kuchokera pamene Yesaya anamwalira.

Ngakhale Yesaya analankhula mwamphamvu za uchimo ndi chiweruzo, Mulungu anamugwiritsanso ntchito kupereka mauneneri ena omveka bwino m'Malemba okhudza Mesiya. Analemba za kubadwa kwa namwali (Yesaya 7:14), Mfumu yaumulungu yomwe idzalamulira kosatha (Yesaya 9:6-7), Nthambi

yolungama yochokera m'nyumba ya Davide (Yesaya 11:1-10), wotsogolera amene adzakonza njira ya Ambuye (Yesaya 40:3-5) ndiponso munthu wazisoni amene adzavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu ndipo adzanyamula machimo a ambiri (Yesaya 53). Maulosi awa akusonyeza momveka bwino kubwera kwa Yesu Khristu.

Baibulo silimanena mmene Yesaya anafera. Malinga ndi zolemba zakale za Ayuda ndi Akhristu, iye anaphedwa ali ndi zaka 90 panthawi ya ulamuliro wa Manase ndipo anachekedwa pakati m'magawo awiri, apa ena amakhulupirira kuti izi zikuonetsedwa mu Ahebri 11:37. Ngakhale izi sizingatsimikizidwe kuchokera m'Malemba, zikuonetsa kuopsa kwa zomwe anakumana nazo aneneri omwe sanafune kupeputsa uthenga wa Mulungu.

Yesaya anaulula chikhalidwe chenicheni cha uzimu wa Yuda, komabe anasenza uthenga wa chiyembekezo. Anakumbutsa anthu za chiyero cha Mulungu ndi kuwatsogolera kwa Mpulumutsi amene adzabwera. Zolemba zake, zodziwika bwino chifukwa cha kalembedwe kake kozama komanso ka ndakatulo, zimapereka chithunzi chimodzi chomveka bwino cha Mesiya mu Chipangano Chakale. Iye ndiye mneneri amene zolemba zake zimatchulidwa kwambiri mu Chipangano Chatsopano. ■

# ZEFANIYA

## MNENERI WA TSIKU LA AMBUYE



***MASIKU:*** Anatumikira pafupifupi 640–621 BC

***NTCHITO:*** Mneneri

***MALO:*** Yuda, makamaka Yerusalemu

***BUKU:*** Zefaniya

***MITU:*** Tsiku la Ambuye, chiweruzo pa uchimo, chiyero cha Mulungu, kulapa, kubwezeretsedwa, otsalira amene ayeretsedwa

Zefaniya (kutanthauza *"wobisika ndi Yehova"*) anatumikira ku Yuda panthawi ya ulamuliro wa Mfumu Yosiya (Zefaniya 1:1), mwina mfumu isanayambe kusintha chipembedzo. Mbadwo wake unachokera m'mibadwo inayi mpaka kufika pa "Hezekiya," ndipo akatswiri ambiri amakhulupirira kuti apapa akutanthauza Mfumu Hezekiya. Ngati kulumikizanaku kuli kolondola, Zefaniya anali wochokera m'banja lachifumu, zimene zili zosowa kwambiri kwa mneneri, ndipo uthenga wake unali ndi mphamvu zodabwitsa pamene anaitana Yuda kuti abwerere kwa Mulungu.

Pamene Zefaniya anayamba kulankhula, Yuda anali atayamba kulowerera kuuuzimu ndipo anali ataipitsidwa kwambiri. Kulambira mafano kunali kutafalikira, chiwawa ndi chisalungamo zinali paliponse, ndipo anthu ambiri anali samadzidzimuka ndi machimo awo. Zefaniya anayamba uneneri wake ndi chenjezo lomveka bwino lakuti chiweruzo cha Mulungu chinali kuyandikira. M'buku lonselo, akunena za "tsiku la Yehova" yomwe ili nthawi imene Mulungu adzathana ndi uchimo mu Yuda ndiponso mitundu yozungulira (Zefaniya 1:14-18). Mau ake akuphatikizapo kufotokoza mwamphamvu za chiweruzo mu Chipangano Chakale, chomwe cholinga chake chinali kudzutsa anthu ku kulekerera kuuzimu.

Koma uthenga wa Zefaniya sukungonena za chiweruzo chokha basi. Iye anauza Ayuda kuti afunefune Yehova, afune chilungamo ndipo adzichepetse, nawalonjeza kuti Mulungu adzasunga otsala omwe adzamukhulupirire (Zefaniya 2:3). Analengezanso chiweruzo pa mitundu yozungulira monga Filistiya, Mowabu, Amoni, Kusi, ndi Asuri kuwakumbutsa kuti Mulungu amalamulira mitundu yonse.

Bukuli likumaliza ndi kusintha kuchoka pa chiweruzo kupita ku kubwezeretsa. Zefaniya analosera za tsiku limene Mulungu adzayeretse anthu ake, kuwachotsa mantha ndi manyazi awo, ndi kuwasonkhanitsanso. Limodzi mwa malonjezo odabwitsa a Chipangano Chakale likupezeka apa: **"Yehova Mulungu wako ali pakati pako, wamphamvu wakupulumutsa... adzasekerera nawe ndi kuyimbirapo"** (Zefaniya 3:17).

Malemba salemba chilichonse chokhudza imfa ya Zefaniya, ndipo zochepa zomwe zimadziwika za moyo wake atamwalira iyeyo. Koma uthenga wake uli ngati umodzi mwa maitanidwe omaliza kwa Yuda Ababiloni asanafike kudzaononga. Zefaniya akutikumbutsa kuti chiyero cha Mulungu chiyenera kuonedwa mozama, koma chifundo chake chimaperekedwa kwa onse amene adzichepetsa ndi kubwerera kwa Iye. ■

# HABAKUKU

## MNENERI WOFUNSA MAFUNSO



**MASIKU:** Anatumikira pafupifupi 612–600 BC

**NTCHITO:** Mneneri

**MALO:** Yuda

**BUKU:** Habakuku

**MITU:** Chilungamo cha Mulungu, mafunso ndi chikhulupiriro, chiweruzo pa zoipa, kukhala ndi moyo mwa chikhulupiriro, ulamuliro wa Mulungu

Habakuku (kutanthauza *"iye amene amakumbatira"*) anakhala ku Yuda m'zaka zomwe Ababiloni anaukira, mwina panthawi ya ulamuliro wa Yehoyakimu. Buku lake, lolembedwa mu nthawi yomweyi ya utumiki wa Yeremiya, ndi lachilendo pakati pa aneneri: m'malo mwa maulaliki kwa anthu, limalemba zokambirana ndi Mulungu. Ndicho chifukwa chake nthawi zambiri amakumbukiridwa ngati *"mneneri wofunsa mafunso."* Anayang'ana chiwawa, chisalungamo, ndi kuchepa kwauzimu kwa mtundu wake, ndipo anabweretsa nkhawa zake mwachindunji kwa Ambuye (Habakuku 1:2-4).

Yankho la Mulungu linali losayembekezereka. Anaulula kuti Babiloni adzauka kuti aweruze Yuda (Habakuku 1:6). Izi zinabweretsa funso lina kwa Habakuku, kuti kodi Mulungu angagwiritse ntchito mtundu woipa kwambiri kuposa Yuda? Komabe Ambuye anamukumbutsa kuti Iye amalamulira mitundu yonse ndipo kuti uchimo, kaya uli ku Yuda kapena ku Babiloni, sudzathawa chiweruzo chake. Koma pankhaniyi pali choonadi chachikulu chakuti: "Wolungamayo adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro chake" (Habakuku 2:4), ndipo mau awa anabwereza kambirimbiri mu Chipangano Chatsopano.

Bukuli likumaliza ndi pemphero lomwe likhale kulengeza za chikhulupiriro. Habakuku akuyamba ndi mafunso koma akumaliza ndi kudzidalira: "Koma ndidzakondwera mwa Yehova, Ndidzasekerera mwa Mulungu wa chipulumutso changa" (Habakuku 3:18). Mau ake omaliza akusonyeza kuti chikhulupiriro sichitsamira pa zimene munthu wakumana nazo mwa koma Mulungu amene sasintha. Tanthauzo la dzina la Habakuku limafanana ndi utumiki wake wauneneri. Iye anakakamira pa Mulungu m'pemphero ndi chikhulupiriro ngakhale pamene anali ndi mafunso okhudza machitidwe a Mulunguyo.

Malemba samanena za imfa ya Habakuku, ndipo palibe china chilichonse chodziwika bwino chokhudza moyo wake. Habakuku analimbana ndi mafunso omwe amakumana nawo okhulupirira masiku ano, akuti ndi chifukwa chiyani Mulungu amalola zoipa, mmene chilungamo chake chimagwirira ntchito, ndi kupirira kwa chikhulupiriro munthawi yosatsimikizika. Habakuku akuonetsa kuti kufunsa mafunso ovuta si kusakhulupirira koma ndi njira yodalira Mulungu mozama. ■

# YEREMIYA

## MNENERI WOLIRA



**MASIKU:** Anatumikira pafupifupi 626–586 BC

**NTCHITO:** Mneneri ndi wansembe

**MALO:** Anatoti ndi Yerusalemu; Yuda

**BUKU:** Yeremiya; Maliro

**MITU:** Chiweruzo, kulapa, kukhulupirika pa pangano, kugwa kwa Yuda, kubwezeretsedwa ndi chiyembekezo

Yeremiya (kutanthauza kuti *"Ambuye amasankha/amakweza/amagwetsa"*) anali mwana wa Hilikiya, wansembe wochokera ku mudzi wa Anatoti m'dziko la Benjamini (Yeremiya 1:1). Kuitanidwa kwake kunabwera m'chaka cha khumi ndi chitatu cha Mfumu Yosiya, cha m'ma 627 BC, pamene Mulungu anamuuza kuti, "Ndisanakulenge m'mimba ndinakudziwa … Ndinakuika kukhala mneneri wa mitundu ya anthu" (Yeremiya 1:5). Yeremiya anaitanidwa ali wamng'ono kwambiri, zomwe zinaonekera m'mau ake enieni: "Ndili mwana" (Yeremiya 1:6). Utumiki wake unayamba pasanathe zaka 100 kuchokera pamene utumiki wa Yesaya unatha. Yuda sanamvere machenjezo oyambirira, ndipo dzikolo linali pafupi kuonongedwa komaliza. Yeremiya ananyamula uthenga wa Mulungu m'zaka zomaliza za mbiri ya Yuda. Anatumikira mu ulamuliro wa Yosiya, Yehoahazi, Yehoyakimu, Yehoyakini, ndi Zedekiya, mpaka kuonongedwa kwa Yerusalemu mu 586 BC. Utumiki wake unatenga pafupifupi zaka makumi anayi.

Nthawi zambiri Yeremiya amatchedwa *"mneneri wolira"* chifukwa cha chisoni chachikulu chomwe anali nacho chifukwa cha tchimo la Yuda ndi chiweruzo chomwe chinali kubwera. Olemba mbiri ochuluka amamufotokoza ngati wolingalira mozama

komanso wosautsidwa mtima kwambiri. Ngakhale kuti nthawi zambiri ankavutika ndi kulemera kwa uthengawo ndipo nthawi zina naoneka ngati wokhumudwa—anakhalabe womvera komanso wokhulupirika ku kuitana kwa Mulungu. Mulungu anamutuma kuti akachenjeze dzikolo kuti Babiloni adzagonjetsa Yerusalemu chifukwa anthuwo anali ataumitsa mitima yawo ndikuyamba kulambira mafano. Yeremiya anawapempha kuti alape, koma uthenga wake unakanidwa mobwerezabwereza. Aneneri onyenga anamutsutsa ndipo analonjeza mtendere pamene panalibe mtendere (Yeremiya 6:14). Anthu anamunena Yeremiya kuti ndi wopanduka, pamene anawauza kuti asalimbane ndi Babiloni, chifukwa Mulungu anali atapereka Yuda m'manja mwa Nebukadinezara.

Yeremiya anavutika kwambiri chifukwa cha uthenga umene Mulungu anamuuza kuti alankhule. Anamenyedwa, anamangidwa, ndipo anaponyedwa m'chitsime momwe anamira m'matope (Yeremiya 38:6). Mfumu Yehoyakimu anang'ambanga mpukutu wa ulosi wolembedwa wa Yeremiya ndipo anautentha pang'onopang'ono (Yeremiya 36). Yerusalemu atagwa, Yeremiya anakhala ndi anthu ochepa omwe anatsala m'dzikolo. Pambuyo pake otsalawo anamukakamiza kupita nawo ku Igupto, ngakhale kuti anawachenjeza kuti asathawire kumeneko (Yeremiya 42–43). Baibulo silinenapo chilichonse chokhudza imfa yake, ngakhale kuti mwambo wa pambuyo pake umati anaponyedwa miyala ku Igupto.

Pakati pa mavuto onsewa, Mulungu anapatsa Yeremiya uthenga wopatsa chiyembekezo. Ananeneratu kuti Mulungu adzachita pangano latsopano ndi anthu ake, kulemba malamulo ake m'mitima yawo

(Yeremiya 31:31-34). Ngakhale kuti Yeremiya anakhala ndi moyo mpaka kuona kuwonongedwa kwa Yerusalemu, analengezanso kuti Mulungu adzabwezeretsa anthu ake.

Utumiki wa Yeremiya umadziwika bwino chifukwa cha kuona mtima kwake, chifundo chake, ndi kupirira kwake. Iye anaulula tchimo la Yuda, anachenjeza za chiweruzo chomwe chikubwera, ndipo analozerabe ku chifundo cha Mulungu ndi lonjezo la pangano latsopano lomwe tsiku lina lidzakwaniritsidwa mwa Khristu. ■

# EZEKIELE

## MNENERI WAULONDA



***MASIKU:*** Anatumikira pafupifupi 593–571 BC

***NTCHITO:*** Mneneri ndi wansembe

***MALO:*** Ukapolo ku Babiloni; pakati pa akapolo pafupi ndi Mtsinje wa Kebara

***BUKU:*** Ezekiele

***MITU:*** Ulemerero wa Mulungu, chiweruzo pa Yuda, chiweruzo pa mitundu, udindo wa munthu payekha, kubwezeretsedwa, mtima watsopano ndi mzimu watsopano

Ezekiele (kutanthauza *"mphamvu ya Mulungu"*) anali wansembe komanso mwana wa Buzi. Anatengedwa kuchokera ku Yerusalemu kupita ku Babiloni panthawi ya kutengedwanso kwachiwiri mu 597 BC (Ezekiele 1:1–3). Ezekiele anatengedwa Yerusalemu asanaonongedwe komaliza, ndipo utumiki wake unachitikira pakati pa akapolo omwe ankakhala pafupi ndi mtsinje wa Kebara. Ngakhale kuti anali kutali ndi Yerusalemu, Mulungu anamugwiritsa ntchito kulankhula ndi akapolo achiyuda ochokera ku Yuda omwe, ngakhale atachenjezedwa ndi Yesaya ndi Yeremiya, sanamvetsebe kuopsa kwa tchimo lawo kapena cholinga cha ukapolo wawo.

Ezekiele anaitanidwa ngati mneneri m'chaka chachisanu cha Mfumu Yehoyakini, cha m'ma 593 BC (Ezekiele 1:2). Iye anaona masomphenya odabwitsa a ulemerero wa Ambuye ndipo masomphenyawo ndi amene adamanga maziko a utumiki wake wonse. Chifukwa Mulungu adamuika kukhala "mlonda wa nyumba ya Israele" (Ezekiele 3:17), Ezekiele nthawi zambiri amadziwika kuti "mneneri waulonda." Akatswiri amamufotokozanso kuti ndi "mneneri wa masomphenya" chifukwa cha mauneneri ake achindunji komanso a zinthu zooneka mwazithunzi komanso "mneneri wa ukapolo" chifukwa utumiki wake wonse unachitikira ku Babiloni. Olemba mbiri yakale amamulongosola Ezekiele ngati munthu wodzipereka kwambiri kwa Mulungu komanso wodziwa bwino masomphenya ake, komanso chifukwa cha maonekedwe odabwitsa ndipo pena osamvetsetseka a masomphenya ake.

Ezekiele anatumikira nthawi yofanana ndi ya Daniele, amene anatengedwa ukapolo koyambirira m'chaka cha 605 BC. Ngakhale kuti anatumikira m'malo osiyanasiyana; Daniele m'bwalo lachifumu ndi Ezekiele pakati pa akapolo wamba, Ezekiele anamutchula Daniele kuti anali munthu wolungama komanso wanzeru (Ezekiele 14:14, 20; 28:3).

Mu utumiki wake woyamba, Ezekiele anachenjeza kuti Yerusalemu adzaonongedwa chifukwa anthu anakana kulapa. Uthenga wake unali wolimba komanso wolunjika, ndipo nthawi zambiri Mulungu ankamulamula kuti achite zizindikiro zophiphiritsira kuti afotokoze chiweruzo chomwe chikubwera. Ezekiele anagona

chagada kwa masiku ambiri kuti aimire zaka za uchimo wa Israele ndi Yuda (Ezekiele 4:4-6). Iye anadya chakudya chophikidwa pa ndowe za anthu kuti afotokoze za kuipitsidwa ndi njala zomwe anthu adzakumana nazo panthawi ya kuzunguliridwa (Ezekiele 4:12-13). Anameta tsitsi lake ndi ndevu zake ndipo anazigawa m'magawo kuti asonyeze tsogolo la Yerusalemu kuti ena adzatenthedwa, ena adzakanthidwa ndi lupanga, ndipo ena adzabalalitsidwa ndi mphepo (Ezekiele 5:1-4). Zizindikiro zonsezi cholinga chake chinali kudabwitsa akapolowo kuti adzuke ndi kuopsa kwa mkhalidwe wawo. Pamene Yerusalemu anagwa mu 586 BC, wothawa kwawo anafika ndi nkhaniyo, kutsimikizira zonse zomwe Ezekiele analosera (Ezekiele 33:21). Kuyambira pamenepo, uthenga wake unasintha kuchoka pa chiweruzo kupita ku chiyembekezo. Analankhula za kubwezeretsedwa, mtima watsopano ndi mzimu watsopano (Ezekiele 36:26), ndi lonjezo lakuti tsiku lina Mulungu adzasonkhanitsanso anthu ake.

Ezekiele anali wokwatira, ndipo imfa ya mkazi wake inakhala chizindikiro chachikulu kwa anthu (Ezekiele 24:15-18), ngakhale kuti Malemba sapereka tsatanetsatane wokhudza banja lake.

Ezekiele ananenanso chiweruzo cha Mulungu motsutsana ndi mitundu yozungulira Israele ndipo analandira masomphenya omwe anasonyeza zomwe Mulungu adzachita ndi anthu ake. Masomphenya ake a chigwa cha mafupa ouma gwaa! (Ezekiele 37) ndi chimodzi mwa zithunzi zomveka bwino za Mulungu pamene akubweretsa moyo ndi chiyembekezo pomwe panali imfa yokhayokha. Mutu waukulu mu utumiki wa Ezekiele unali ulemerero wa Ambuye. Anaona ulemerero ukuchoka m'kachisi chifukwa cha uchimo wa Israele, komanso anaona lonjezo lakuti ulemerero wa Mulungu udzabweranso mtsogolo.

Malemba sanena mmene Ezekiele anafera. Zolemba za Ayuda zimati mwina anaphedwa ndi akaidi anzake chifukwa chodzudzula mchitidwe wolambira mafano. Chomwe tikudziwa ndichakuti Ezekiele anakhalabe wokhulupirika ku kuitana kwa Mulungu mu nthawi ya mdima waukulu. Anakumana ndi tchimo lomwe linabweretsa chiweruzo, ndipo anatsogolera anthu ku chiyembekezo cha kubwezeretsedwa kwa Mulungu. ■

# DANIELE

## MNENERI WOLOSERA ZOCHITIKA MTSOGOLO



***MASIKU:*** Anatumikira kwambiri pafupifupi 605–536 BC

***NTCHITO:*** Mneneri ndi mtsogoleri wa boma

***MALO:*** Yerusalemu; Babiloni

***BUKU:*** Daniele

***MITU:*** Mulungu ali wolamulira pa zonse, kukhulupirika mu ukapolo, masomphenya aulosi a maufumu, ulosi wa zakutsogolo, kupulumutsidwa, Mesiya amene akubwerayo

Daniele (kutanthauza kuti *"Mulungu ndiye woweruza wanga"*) anatengedwa ukapolo ku Babiloni mu ndi gulu loyamba kutengedwa ukapolo mu 605 BC, pamene Nebukadinezara anatenga anyamata ochokera ku Yuda omwe anali "a maonekedwe okoma, ndi a luso la nzeru zonse," (Daniele 1:3–4). Akatswiri ambiri amakhulupirira kuti Daniele anachokera m'banja lolemekezeka kapena lachifumu, kutengera lamulo la mfumu loti abweretse akalonga ndi akuluakulu ku bwalo la mfumu ya ku Babiloni. Daniele mwina anali wachinyamata pamene anafika ku Babiloni, koma anapanga chisankho mumtima mwake kuti asadzidetse ndi chakudya cha mfumu (Daniele 1:8). Kuyambira pachiyambi, Daniele anakhalabe wodzipereka kwa Mulungu.

Daniele anatumikira pansi pamafumu angapo; Nebukadinezara, Belisazara, Dariyo Mmedi, ndi Koresi ndipo Mulungu anamugwiritsa ntchito pa maudindo a utsogoleri m'maufumu onse a ku Babiloni ndi oyambirira a Perisiya. Pa kusintha konse ndi mavuto okhala m'dziko lachikunja, anakhalabe wokhulupirika kwa Mulungu. Daniele ankapemphera nthawi zonse, anafunafuna nzeru za Mulungu, ndipo anakana kusiya ngakhale pamene anaopsezedwa kuti adzafa. Mu ulamuliro wa Dariyo, Daniele anaponyedwa m'dzenje la mikango chifukwa chopitiriza kupemphera kwa Mulungu, ndipo Ambuye anamupulumutsa (Daniele 6).

Daniele amadziwika ndi masomphenya ake okhudza chiwonongeko. Mulungu anaulula maufumu amtsogolo, kukwera ndi kugwa kwa mitundu, ndi kukhazikitsidwa kwa ufumu wosatha wa Khristu. Kutanthauzira kwake maloto a Nebukadinezara (Daniele 2 ndi 4), masomphenya ake a zilombo zinayi (Daniele 7), ndi uneneri wake wa nkhosa yamphongo ndi mbuzi (Daniele 8) kumavumbula ulamuliro wa Mulungu ndipo kumaloza ku ufumu wa Khristu. Masomphenya awa, ndi kutanthauzira kwa Daniele koperekedwa ndi Mulungu, zimathandiza kumasulira tanthauzo la uneneri wofanana nawo wopezeka ku Chivumbulutso.

Pemphero la Daniele mu mutu 9 ndi chimodzi mwa zithunzi zomveka bwino zomwe tili nazo zokhudza kupempherera mtundu wochimwa. Mu mutu womwewo, Mulungu adamupatsa ulosi wa "masabata makumi asanu ndi awiri," womwe unkalozera mosakayikira za kubwera kwa Mesiya (Daniele 9:24-27).

Daniele anakhala ndi moyo nthawi yomweyi ndi Ezekiele. Ezekiele amatchula Daniele ngati munthu wolungama komanso wanzeru (Ezekiele 14:14, 20; 28:3), zomwe zikusonyeza kuti kukhulupirika kwa Daniele kunali kodziwika ngakhale kwa akapolo ena.

Daniele nayenso anaona kugwa kwa Babiloni. Pa phwando la Belisazara, dzanja la Mulungu linalemba uthenga uwu pakhoma: "Mene, Mene, Tekel, ndi Parsin." Daniele anamasulira izi kuti chinali chiweruzo cha Mulungu pa ufumuwo (Daniele 5). Usiku womwewo, Babiloni anagonjetsedwa ndi Amedi komanso Aperisi.

Baibulo silinena za imfa ya Daniele. Iye anali kutumikirabe m'chaka chachitatu cha Koresi (Daniele 10:1), zomwe zikusonyeza kuti anakhala ndi moyo mpaka ukalamba. Moyo wa Daniele, womwe umadziwika ndi kulimba mtima, ungwiro, nzeru, ndi kudzipereka kolimba kwa Mulungu, umatikumbutsa kuti mosasamala kanthu za ulamuliro wa munthu, tikhoza kukhala mokhulupirika pansi pa ulamuliro wa Mulungu mu ufumu wake. ■

# MIKA

## MNENERI WA CHILUNGAMO CHA ANTHU



***MASIKU:*** Anatumikira pafupifupi 740–687 BC

***NTCHITO:*** Mneneri

***MALO:*** Yuda

***BUKU:*** Mika

***MITU:*** Chilungamo, chifundo, chipembedzo choona, chiweruzo ndi kubwezeretsedwa, Wolamulira wochokera ku Betelehemu amene akubwera

Mika (kutanthauza *"Ndani ali ngati Ambuye?"*) analosera panthawi ya ulamuliro wa Yotamu, Ahazi, ndi Hezekiya. Utumiki wake unachitika nthawi yomweyo monga Yesaya, ndipo uthenga wake ukufanana ndi wa Hoseya komanso Amosi, amene anatsutsa machimo ndi zosalungama za m'zaka za m'ma 700 BC. Mika anachokera ku Moresheti, dera lakumidzi ku Yuda, ndipo analankhula momveka bwino za kulowa pansi kwa zauzimu ndi makhalidwe abwino kwa mtunduwo. Buku lake limanena mobwerezabwereza za chiweruzo, lonjezo, ndi pempho, kusonyeza chiyero cha Mulungu ndi chifundo chake chosatha.

Mika amakumbukiridwa ngati mneneri wa chilungamo cha anthu chifukwa ankachita zinthu mwachindunji ndi machimo omwe ankavulaza osauka ndi ofooka. Anatsutsa anthu omwe ankalanda minda ndi nyumba kuchokera kwa mabanja opanda chitetezo (Mika 2:1-2). Anadzudzula atsogoleri omwe ankagwiritsa ntchito mphamvu zawo molakwika ndipo analephera kusunga chilungamo (3:9). Oweruza, ansembe, ndi aneneri nthawi zambiri ankatumikira kuti alipire, ndipo Mika anavumbulutsa mchitidwe wa chinyengowu, kuti umanyoza Mulungu (3:11). Iye analankhulanso motsutsana ndi kugwiritsa ntchito miyeso ndi masikelo abodza, zomwe zinkanyenga anthu pamalonda a tsiku ndi tsiku (6:10-11). Kudzera mwa Mika, Ambuye anakumbutsa anthu kuti kulambira koona kuyenera kugwirizanitsidwa ndi chilungamo ndi kuchita zinthu mwachilungamo.

Uthenga wa Mika umalozanso za chiyembekezo. Iye analosera kuti Wolamulira adzachokera ku Betelehemu amene adzawete anthu a Mulungu mwa mphamvu ya Ambuye (Mika 5:2-4). Zipatso za ulaliki wake zinaonekera kwa nthawi yaitali; ndipo malingana ndi Yeremiya 26:18-19, chenjezo lake linasowetsa mtendere mtima wa Mfumu Hezekiya ndipo zinathandiza kuti dziko lonse lilape. Mika anafotokoza mwachidule lamulo la Mulungu m'mau awa amene sitiwayiwala: "kuti uchite cholungama, ndi kukonda chifundo ndi kuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wako?" (Mika 6:8). Bukuli likumaliza ndi kutsimikizira mwamphamvu za chifundo ndi kukhulupirika kwa Mulungu. ■